

# KUFUNA BWENZI? KHALA BWENZI!

KALOZERA WAKASAMALIDWE KA AGALU NDI KUPEWA KULUMIDWA



**Developed by:**  
René Grobler, Amanda Klette,  
Netcare Trauma Division  
Daniel Steward & Terence Scott  
Global Alliance for Rabies Control

**Translations Supported by:**



Centre for Community  
Empowerment  
Initiatives (CCEI)



Dierenartsen  
Zonder Grenzen



You're in safe hands




# CHIYANKHULO CHA AGALU GALU WANGA AKUNDIUZA CHIYANI?



Tcheru



Wokayikira



Kuda nkhawa



Kuwopsezedwa



Mkwiyo



Waubwezi




Kufuna danga



Kufuna chikondi



Wokondwa



Kuzembelera



Kutambasulila moni



Waubwenzi



Okonzeka



Mundidyetse



Kusangalala kwambili

© 2011 Lili Chin [www.doggiedrawings.net](http://www.doggiedrawings.net)

*Lili*

# M'mene ana SAYENERA kusewelera ndi agalu

## Ndizophweka, tangolingalirani momwe anthu ayenera kukhalira limodzi

Pewani kudya zakudya za ena



Pewani kuvutitsa agalu pamene akudya

Pewani kuba zidole za ena



Pewani kutenga mafupa kapena zidole za agalu

Pewani kuika nkhope yanu pa nkhope ya munthu wina



Pewani kuika nkhope yanu pa nkhope ya agalu

Pewani kuvutitsa munthu wogona



Pewani kuvutitsa agalu pamene akupuma

Pewani kuvutitsana




Pewani kugwira mchira kapena makutu agalu

Pewani kukwerana kapena kupondanapondana



Pewani kukwera kapena koponda agalu

Pewani zotsinana



Pewani kukumbatira agalu. Agalu ambili sakonda izo


Pewani kukuwa



Pewani kukuwa ndi maphokoso ena aakulu monga ma belo, ng'oma ndi zina Zotero

Poster adapted from resources available by Dr. Sophia Yin at [www.drsophiayin.com](http://www.drsophiayin.com)

# Chekenelani!



# UMWINI WODALIRIKA PA ZIWETO

## MAUFULU ASANU

Ndi udindo wathu kuonetsetsa kuti nyama iliyonse ili ndi:



**1. Chakudya chopatsa thanzi ndi madzi aukhondo**



**2. Malo ogona abwino komanso opeleka chitonthozo**



**3. Chithandizo pamene chiweto chadwala kapena kupweteka**



**4. Ubwenzi ndi ziweto zina zathanzi zoti zizisewera limodzi**



**5. Chisangalalo! Tiyenera kuonetsetsa kuti ziweto zathu sizikuchita mantha kapena kukhumudwa**

# OSADZUTSA GALU YEMWE AKUGONA



## Sangalalani ndikupanga maubwenzi ndi ziweto zanu!

Ndi undindo waukulu komanso mwayi kukhala ndi chiweto. Chiweto chanu ndi gawo la banja lanu, chimodzimodzi mlongo kapena mchemwali wanu. Khalani abwenzi omvana ndi ziweto zanu! Ziweto zanu zikhoza kukhala bwenzi lanu lapamtima ndipo zimatha kusunga zinsinsi!

Mukuyenera kusonyeza ulemu ku nyama zonse, monga m'mene mumachitira kwa mlongo wanu, mchemwali wanu, makolo anu, ndi aphunzitsi anu.

Ngati n'kotheke, pezani sukulu yomwe ingaphunzitse galu wanu maziko a malamulo

**Ngati mukufuna bwenzi, khalani bwenzi!**



You're in safe hands



# ZAKUDYA ZOPATSA THANZI KOMANSO MADZI ABWINO

Nyama zonse monga ife anthu, zimafuna zakudya zopatsa thanzi zomwe zili ndi mavitamini ndi michere yonse yofunika mthupi komanso zabwino zonse zomwe ife anthu timazipeza m'zakudya zathu.

Zakudya zomwe tiyenela komanso zomwe sitiyenela kudyetsa agalu athu:

## ZOYENELA

Nyama yophikidwa ✓  
bwino ✓  
Nyama ya nkhuu ✓  
Nyama ya nsomba ✓  
Masamba ✓  
Zam'gulu la chimanga ✓  
Mbatata ✓

## ZOSAYENELA

Chokoleti ✗  
Mphesa ✗  
Anyezi ✗  
Khofi ✗  
Adyo ✗  
Chingamu ✗  
Mowa ✗



# ZOFUNIKA ZAUMOYO

Nyama zonse zitha kudwala, koma tikhoza kupewa izi!

Nyama zimafuna: **Katemala chaka chilichonse**  
**Mankhwala anjoka zammimba**  
**miyezi ingapo iliyonse**  
**Kuonana ndi adokotala aziweto**  
**kamodzi pa chaka**

Kulera kudzela mu njira yothena ndikofunikira. Izi zizalepheretsa a galu ndi a mphaka kubereka ana ambiri omwe sangathe kusamalidwa bwino.



# KUSAKA MAWU

|   |   |   |   |   |   |   |   |   |   |   |   |   |   |   |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| C | H | I | K | O | N | D | I | A | J | D | Y | C | R | F |
| X | Y | U | A | G | U | C | J | B | Z | X | V | H | Y | E |
| H | J | T | S | N | C | X | A | S | M | C | H | I | R | A |
| F | C | H | I | W | E | W | E | E | V | X | O | W | N | F |
| P | U | A | L | S | F | P | O | W | N | F | P | E | L | S |
| K | V | M | G | X | O | U | J | E | C | N | J | T | G | C |
| U | I | A | U | N | C | B | P | R | G | H | B | O | I | B |
| W | T | N | B | K | N | W | G | A | L | U | A | H | V | T |
| A | N | G | I | U | T | E | U | L | T | W | S | N | X | I |
| O | L | A | X | Y | O | Y | S | A | W | P | J | Z | C | B |
| A | J | F | P | E | A | J | F | V | I | M | P | I | R | A |
| K | U | N | U | N | K | H | I | Z | A | B | L | D | H | N |
| V | B | O | S | D | C | S | J | L | W | C | F | O | S | J |
| L | P | J | I | A | T | V | P | O | G | X | U | L | N | A |
| S | C | T | N | O | X | W | K | A | T | E | M | E | R | A |

**MPIRA**  
**KUWA**  
**FUPA**  
**GALU**  
**BANJA**  
**UBWEYA**  
**CHIKONDI**  
**CHIWETO**  
**SEWERA**  
**THAMANGA**  
**KUNUNKHIZA**  
**MCHIRA**  
**ZIDOLE**  
**KUYENDA**  
**CHIWewe**  
**KATEMERA**  
**PUSI**



# KUPEWA KUPOSA KUCHIZA

## "Lekani Kuluma Zisanachitike"

Agalu sadziwa kuti kuluma ndikolakwika. Nthawi zambiri agalu amaluma ngati ali ndi mantha kapena akuyesera kudziteteza.

Pofuna kupewa kulumidwa ndi agalu, tiyenera kumvetsetsa izi:

- Momwe agalu akumvera mthupi
- Momwe mungayandikire agalu popanda chiophyezo
- Pamene kuli kuli koopsa ndipo sikuli koopsa kuyandikira kapena kucheza ndi agalu

Tingapewe kulumidwa ndi agalu pomvetsetsa khalidwe lawo komanso kupewa mikumano yoopsya,

### ZIZINDIKILO ZOOPSYA

- Thupi losakhazikika
- Mchira woima
- Kubweza makutu
- Kubwerera m'mbuyo
- Kukuwa
- Kudzidzimuka
- Kuyang'ana kwambiri
- Ubweya woyima



### ZOYENERA KUCHITA

- Khalani manja kumbali yanu
- Imani njii



### ZOSAYENERA KUCHITA



- Kuthawa galu
- Kukuwa kapena kuchita mantha
- Kuyang'ana galu m'maso

### NGATI MWALUMIDWA

- Musachoke pamalo pomwe mwalumidwapo
- Ngati mwagwa, zikungeni ngati mpira pokokela manja ndi miyendo ku thupi lanu



# KAPEWEDWE KAKULUMIDWA

## Tingapewe bwanji kulumidwa ndi agalu?

### Kwa agalu omwe timawadziwa:

Pamene ana agalu akadali aang'ono, tiyenera kusewera nawo bwino pafupipafupi kuti asamaope anthu. Ana agalu ayenera kuzolowera kusewera ndi anthu kuti akule mozolowera kukhala bwino ndi iwo owasamala ndipo asazolowele kuluma. Umu ndimomwe tingathe kuzolowelerana ndi agalu athu.

Eni agalu onse ayenera kuphunzira kulankhulana ndikumvana ndi agalu awo, kutero, iwo akoza kupewa makhalidwe owopsa ndi kuphunzitsa agalu awo kukhala ndi makhalidwe abwino pakati pa anthu.

Gwilitsani njira zakulera ngati kuthena paziweto zanu. Agalu aamuna omwe sanathenedwe amatha kukhala aukali kwa nyama zina komanso anthu. Agalu aakazi amatha kudwala ngati sanathenedwe. Kusathena ziweto zanu kungakhale koopsa kwa anthu komanso ziweto zina.

### Kwa agalu omwe sitiwadziwa:

Ngati galu akuthamangira kwa inu, Imani njii ndipo khalani chete. Muloreni galu akununkhizeni ndipo pamene galu wasunthapo- muyenera kuyenda pang'onopang'ono ndi mwakachetechete kuchokapo pamalopo.

Khalani kutali ndi agalu omwe simukuwadziwa. Izi zikuphatikizapo agalu omwe ali omangidwa pa tcheni kapena omwe ali mu mpanda.

Osachita chipongwe, kuthamangitsa, kapena kuponya chilichonse kwa galu. Musasokoneze agalu omwe akudya, kugona, kapena kuyamwitsa ana.

Khalani chelu ndi malo okuzungulirani komaso agalu amene amakhala mu malo amenewa. Pangani nawo ubale agalu okhala mokuyandikilani ndipo lemekezani malo omwe agaluwo amakhala.

Osamenya, kukankha kapena kukalipira agalu, ndipo pewani agalu omwe akuchita zinthu modabwitsa.

# CHIWEWE

## KODI CHIWEWE NDI CHANI?

Chiwewe ndi kachilombo komwe kamakhudza gulu la nyama zonse zoyamwitsa ndipo nthawi zambili, kamapezeka mwa agalu. Popeza kachilomboka kamakhala m'malovu a nyama sonse za m'gulu la nyama zoyamwitsa zomwe zili nako, kamalowa m'thupi la nyama zathanzi komanso anthu potsatira kulumidwa kapena kunyambita zokala ndi mabala pakhungu. Kachilomboka kamatha kupha munthu kapena chiweto ngati mankhwala sanapelekedwe kwa olumidwayo.

Titha kupewa matenda achiwewe popeleka katemela wachiwewe kwa agalu athu:



**Pewani kulumidwa**



**Pewani kutenga agalu osokera**



**Pewani kunyambitidwa kapena kukalidwa ndi galu**

## KODI NDIZOTHEKA KUCHIZA MATENDA A CHIWEWE?

Tiyenera kuyesetsa kupewa matenda a chiwewe popeleka katemela! Zizindikilo za matenda a chiwewe zikangoonekera, sitingathe kuchiza matendawa.

Pali njira zitatu zosavuta zopewera matenda a chiwewe:

1. Pewani kulumidwa ndi nyama iliyonse
2. Ngati mwalumidwa, sambitsani chilondacho nthawi yomweyo ndi madzi oyenda komanso sopo kwa mphindi khumi ndi zisanu
3. Muuzeni munthu wamkulu kuti mwalumidwa chifukwa akuyenera kupita nanu kuchipatala kuti mukalandile katemera wa chiwewe



### ZINDIKIRANI:

Ngati simungapeze munthu wamkulu woti akuperekezeni, pitani ndi bwenzi lanu chifukwa ndikofunikira kuti mupeze chithandizo mwachangu



# Onani Kusiyaana!

(Pali 13 zosiyana)





# KUPEWA CHIWEWE!



**Ngati mwalumidwa ndi galu – sambitsani bala ndikupita kuchipatala!**

**MOMWE MUNGAPEWERE KULUMIDWA NDI GALU!**

- X** Khalani kutali ndi agalu omwe **SIMUKUWADZIWA!**
- X** Khalani kutali ndi agalu omwe akuonetsa khalidwe lachilendo – akhoza kuluma!
- X** Musathamangitse, kumenya, kukankha, kapena kukalipira agalu!
- X** Osalowerera pamene agalu akudya, kugona, kapena kuyamwitsa!





agriculture, environmental affairs  
& rural development  
Department  
Agriculture, Environmental Affairs  
& Rural Development  
PROVINCE OF MZIMBAZI

Concept by: D. Stewart Rabies Project Designed by: D. Cooke Department of Agriculture, Environmental Affairs & Rural Development: Veterinary Epidemiology Section 033 3476267

**INE**



**GALU WANGA**



# ZIKOMO

**Satifiketi iyi yapatsidwa kwa:**

---

**Chifukwa ndikudziwa panopa mmene ndingakhalire  
popanda chiopsezo ndi agalu!**

**Ndikulonjeza kuti:**

- Ndidzafunsa nthawi zonse ndisanayambe kusewera ndi agalu
- Ndidzayang'ana kumbali osati maso ndi maso ndi galu
- "Ndidzakhala ngati mtengo" kapena "ngati mwala"
- Ngati galu osamangidwa akubwera kwa ine
- Osasewera ndi galu ngati akudya, akugona kapena ali ndi ana



You're in safe hands



RABIES ALLIANCE



Centre for Community  
Empowerment  
Initiatives (CCEI)

the  
edgard  
Cooper  
foundation

Dierenartsen  
Zonder Grenzen



